

Chidule Cha Ziphunzitso za Baibulo (Bible Doctrines)

Ziphunzitso za Chikhristu ndi zomwe Baibulo limatiphunzitsa. Kuwerenga ziphunzitso za Chikhristu kumakhala kovuta. Nthawi zina zimautsanzo (mtsutso) kusemphana maganizo. Fotokozerani bwino kuti ophunzira amvetsetse mosavuta. Musamalimbane pa mfundo zazing'ono.

Pamene mukuwerenga phunziroli, onani kuti mwawerenga kale zinthu zina zomwe zikufotokozedwa pamene mumawerenga Chipangano Chakale and Chipangano Chatsopano. Ziphunzitso za Chikhristu zimafotokoza ziphunzitso zopezeka m'Baibulo malo osiyanasiyana ndipo ziphunzitsozi zimafotokozedwa mwachidule kuti timvetse mfundo zikuluzikulu za m'Baibulo.

Chiyambi

I. Chipembedzo

1. Tanthauzo la Chipembedzo

- A. Kutumikira ndi kupembedza Mulungu
- B. Kukangalika kuchikhulupiliro ndi katumikiridwe kathu
- C. Ndongomeko ya chikhulupiliro yomwe imachitika mwachidwi ndi chikhulupiliro

Izinso zimachitika ngakhale ndi zipembedzo zabodza monga Chisilamu komanso chipembedzo choona monga Chikhristu. Asilamu amakhulupilira kwambiri mulungu wawo wabodza kotero amakhodza kudzipha okha pomutumikira iye. Akhristu amakhulupilira kwambiri Mulungu wao oona kotero anthu ena amatumikira kwambiri monga mamishonare.

- 2. Dera lililonse padziko lapansi kuli chipembedzo chifukwa komwe kuli anthu kumapezeka chipembedzo. Munthu wina aliyense amadziwa kufunikira kokhala chifupi ndi Mulungu.
- 3. Maonekedwe a chipembedzo. Kodi chipembedzo m'chiyani? Nanga chimaoneka bwanji?
 - A. Timakhudwidwa ndi kudzipereka tokha kwa Mulungu makamaka pakuthokoza ndi kugwira ntchito za chikondi. Mulungu ndi amene amatitsogolera pa kapembedzedwe ndi katumikiridwe koono (Deutronomo 10:13-13, Masalimo 111:10, Mlaliki 12:13 ndi Yohani 6:29.
 - i. Chomwe muyenera kudziwa: Chipembedzo choona ndi pamene Mulungu akutitsogolera, koma vuto ndi lakuti munthu amafuna kusankha m'mene iye akufunira. Tinenenso kuti, munthu amafuna kulenga milungu yake yake. Zitsanzo zina; zikhulupiliro za ziwanda ndi Chisilamu. Chipembedzo choona chimachokera

- kwa Mulungu yekha. Genesis 1:27 akutifotokozera kuti Mulungu analenga ife m'chifanizo chake ndipo anapatsa ife mphamvu yoyanjana ndi Iye.
4. Chipembedzo chimakhudza mtima wathu. Mulungu safuna chipembedzo chakandiona maso (chachinyengo). Mulungu akufuna chipembedzo choona cha mumtima mwathu (Miyambo 4:23 ndi Amosi 5:21-24).
 - A. M'Chipangano Chatsopano, chipembedzo ndiko kumvera zomwe Uthenga Wabwino ukunena osati ntchito za lamulo ndipo tikuyenera kukhulupilira ndi kukhala woyera. Izitu zikutanthauza kuti chipembedzo chimachokera kwa Mulungu yemwe anabvumbulutsa yekha kwa munthu; munthu sakanatha kudziwa Yesu akanakhala kuti Mulungu sanathandizirepo.
 5. Chiyambi cha Chipembedzo
 - A. Chipembedzo monga mwa chilengedwe. Anthu amapanga chipembedzo chawo. Zitsanzo ndi Chisilamu ndi ufiti.
 - B. Chipembedzo monga mwa Baibulo (Mau a Mulungu). Chipembedzo choona chimachokera kwa Mulungu. Kumbukirani munthu wa mwamuna ndi mkazi oyamba anali ndi ubale ndi Mulungu omwe unkatsogozedwa ndi Mulungu mwini.

II. Chibvumbulutso

Bvumbulutso ndi limene limatipangitsa ife kudziwa Mulungu. Mau oti chibvumbulutso amatanthauza kuika poyera zomwe zinabisidwa. Mulungu amazibvumbulutsa Yekha kwa ife. Mulungu amazibvumbulutsa Yekha kwa ife m'njira ziwiri: M'njira ya Chilengedwe ndi njira ya Mau ake Baibulo).

- A. M'njira ya chilengedwe. Anthu onse amadziwa izi m'njira ya chilengedwe. Izi zimafika kwa anthu onse muzomwe zikuoneka, mphamvu ndi ndondomeko zina za chilengedwe m'nzeru ndi mbiri (Masalimo 19:1-6, Aroma 1:19, 20; 2:14, 15). Njira ya chilengedwe siipereka chidziwitso chenicheni cha Mulungu ndi zinthu za uzimu pakutero siitipatsa ife maziko eni eni omwe tikhoza kumangapo pa zatsogolo lathu. Njirayi siyokwanira kuchipulumutso cha munthu.
 - i. Bvumbulutso la chilengedwe ndi zomwe ife timazona mwa Mulungu m'mphamvu ya chilengedwe chake. Chilengedwe chimabvumbulutsa kuti kuri Mulungu; komatu ndi zosakwanira kuti tingapulumsidwe chifukwa sitiona Yesu m'chilengedwe (Masalimo 19:1&2, Aroma 1:18-20. Kuyang'ana kwathu kwa chilengedwe kumatitsimikizira zakuti kuri Mulungu; koma sitingathe kumpeza Yesu m'chilengedwemo.
- B. Bvumbulutso lapera (Baibulo) ndi bvumbulutso limene limabvumbulutsa Mulungu kupyolera m'Baibulo lomwe limatiphunzitsa ife njira ya chipulumutso kupyolera mwa m'dzina la Yesu. Mau a Mulungu (Baibulo) amatiuza kuti Mulungu ndi amene analemba Baibulo, ndipo kuti Baibulo ndi Mau eni eni a Mulungu (Numeri 12:6-8, Aheberi 1:1 ndi 2 Petro 1:21).

- i. Kufunikwa kwa Bvumbulutso la padera. Munthu atatha kugwa m'chimo, zinthu zonse zinasokonezeka pamodzi ndi munthu yemwe; kotero kunali kofunika kuti Mulungu akamasulirensa choonadi cha chilengedwe pakupereka bvumbulutso latsopano la chiombolo lomwe likhoza kuombola ku mphamvu ya uchimo. Kunali kofunika kuti munthu aomboleredwe kupyolera m'bvumbulutso latsopanoli. Tikhoza kuphunzira za Yesu kupyolera m'Baibulo ndipo chidziwitso chimenechi m'chofunika kwambiri kuchombolo (Aroma 10:9-10).
 - ii. Njira zimene Mulungu anagwiritsira ntchito m'Bvumbulutso lake lapadera:
 - a. Fiofane: Kutanthauza kuti Mulungu ankazibvumbulutsa yekha podzionetsera mosiyanasiyana monga m'moto ndi utsi wa mitambo (Exsodo 3:2, 33:9; Masalimo 78:14; 99:7; m'mphepo ya namondwe Yobu 38:1; Masalimo 18:10-16 ndi m'mphepo ya yaziyazi 1 Mafumu 19:12).
 - b. Pakulankhulana mwachindunji, nthawi zina Mulungu ankankhula m'mau omveka bwino kwa anthu. Kumbukirani Mose akuti kwa ana a Israeli Deutronomo 5:4. Nthawi zina ankapangitsa aneneri kulingalira za uthenga wa Mulungu pomwe Mzimu Woyera anali kugwira ntchito m'mitima yawo, 1 Petro 1:11. Nthawi zina ankaonekera m'maloto ndi masomphenya (Numeri 12:6; 27:21; Yesaya 6. Chipangano Chatsopano chimatiphunzitsa kuti Yesu anali ngati Mphunzitsi wankulu ochokera kwa Mulungu kudzabvumbulutsa chifuniro cha Atate (Yohani 14:26).
 - c. Zozwizitsa. Zozwizitsa za Baibulo siziyenera kutengedwa ngati zinthu zongodabwitsa zomwe anthu ankangodabwanazo; komatu zinali zinthu zofunikira kwambiri pa bvumbulutso la padera la Mulungu. Cholinga cha zozizwitsa chinali kufuna kutsimikizira utumiki wa Yesu Khristu ndikuwaonetsa kuti Iye anali ndani. Chozizwitsa chinali chinthu chomwe chinali kuchitika chomwe sichinkachitika m'moyo watsiku ndi tsiku monga kuukitsa munthu kwa akufa. Izi zinali kuchitidwa ndi munthu osakhidwa ndi Mulungu kapena Mulungu mwini. Cholinga cha zozwizitsazo chinali chakuti anthu akhulupilire Yesu ndi kulimbikitsa chikhulupiliro chao (Yohani 11:44-45; Machitidwe 9:36-42. Yesu akuchitabe zozwizitsa lero lino, komatu makamaka mwa kusankha kwake. Ambiri mwa ife timakumana ndi zozwizitsa m'moyo wanthu. Dziwaninso kuti ntchito iriyonse yachipulumutso ndi chozizwitsa.
- iii. Mau a Mulungu ndi njira yokhayo imene Mulungu amazibvumbulutsira kwa ife. Zonse zomwe timadziwa za Mulungu timazipeza m'Baibulo. Sitidziwa china chirichonse za Mulungu pokhapokha titachipeza m'Baibulo. Baibulo lonse ndi Mau a Mulungu; liribe cholakwika chirichonse ndipo liri ndi ulamuliro (1 Akolinto 2:13, 2 Timoteo 3:16). Baibulo ndi lokwanira (Chibvumbulutso 22:18-19). Kumbukirani kuti muyenera kukhulupilira zomwe Baibulo likufotokoza za Mulungu ndipo muyenera kuphunzitsa zokhazo zomwe Baibulo likufotokoza.
 1. Mau a Mulungu ndi Baibulo. Pamene tikulankhula za Mau a Mulungu tikutanthauza Mau obvumbulustidwa ndi Mulungu. Chiri chonse chomwe chiri m'Baibulo ndi Mau a Mulungu, ndipo linauziridwa ndi Mulungu mwini. Baibulo lonse ndi lamulo losalakwika la Mulungu ndipo liri ndi zomwe anthu onse ayenera kuchita. Tiyenera kumvera zonse zomwe ziri m'Baibulo. Olemba Chipangano Chakale ankauzidwa mobwerezabwerez

kuti alembe zomwe Mulungu ankawalamulira kuti alembe: Eksodo 17:14; 34:27; Numeri 33:2; Yesya 8:1, 30:8; Yereimeiya 25:13, 30:2; Ezekieli 24:1; Daniel 12:4; Habakuku 2:2; 2 Timoteo 3:16 amatsimikizira kuuziridwa ndi ulamuliro wa Baibulo.

2. Nanga Mau a Mulungu anauziridwa bwanji

A. Pali maganizo awiri olakwika za kuuziridwa kwa Mau a Mulungu

- i. Kuuziridwa mwachindunji. Apa ena amati Mulungu ankawauza olemba Baibulo zomwe olembawo ankalembe ndipo iwo sankaganiza chirichonse anali ngati cholemba m'dzanja la wolemba. Apatu ganizo limakhala lakuti olemba sanaganize chirichonse pa china chirichonse ankalembecho. Izi sizoonza chifukwa alipo olemba ena omwe ankasokhanitsa zomwe ankalembezo kuzolembedwa ndi anza (1 Mafumu 11:41; 14:29; 1 Mbiri 29:29; Luka 1:1-4). Kachiwiri, m'malo ena ankalembe zomwe iwo anakumana nazo ndi kuziona izi timazona m'buku la Masalimo.
- ii. Sanauziridwe mwachindunji. Apa ena amati olemba maganizo ndi mzimu wa olemba unkalimbikitsidwa ndi kukwezedwa m'mwamba ndipo ankaona zinthu mosavuta ndipo ankaona zinthuzi mwachinsinsi.

B. Zoonza zake za kuuziridwa ndi zakuti Mzimu Woyera ankagwira ntchito pa wolemba Baibulo m'njira yogwirizana ndi zomwe iwo anali kudziwa ndi m'mene iwo analiri, nzeru, mphatso, maphunziro, miyambo, chilankhulo ndi luso lao. Mzimu Woyera ankaunikira mitima yawo, kuthandizira chikumbu mtima chao, zinkawapangitsa kulemba, motsutsana ndi machimo ao polemba pakuwalondolera iwo m'kaganizidwe kao ngakhalenso kusankha kwa mau omwe iwo anali kulemba. Baibulo ndi Mau a Mulungu.

C. M'mene Baibulo linauziridwira

- i. Kuganizira kuti magawo ena a Baibulo ndi Mau a Mulungu koma ena ayi ndi kulakwitsa kwakuru chifukwa uku nkukana kuti Baibulo linauziridwa ndi Mulungu. Kaganizidwe aka kamaphunzitsa kuti magawo ena a Baibulo sanauziridwe ndi Mulungu. Uku m'kulakwitsa kwambiri chifukwa Mau ena alionse a m'Baibulo anuziridwa ndipo ndi Mau eni eni a Mulungu.
- ii. Zoonza ndi zakuti Baibulo lonse linauziridwa ndipo ndi Mau a Mulungu, izitu zikutanthauza mau alionse omwe ali m'Baibulo: Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano. Yesu Khristu ndi atumwi ankagwiritsa ntchito kwambiri Chipangano Chakale ndi Chatsopano ngati Mau a Mulungu pofuna kupeza yankho pamtsutso ulionse (2 Petro 3:16, 2 Timoteo 3:16).

3. Choonadi chosanthika ndi mau amene amafotokoza za ulamuliro wa Baibulo. Awa ndi mabuku amene mpingo unavomereza kuti ndiwo Mau a Mulungu.

iii. Chiphunzitso cha Mulungu

1. Kodi maonekedwe a Mulungu ndi otani? Mpovuta kufotokoza za maonekedwe a Mulungu, komatu ndi kosavuta kufotokoza za m'mene tingamuonere Mulungu. Mulungu ndi Mzimu opanda malire ndi wangwiro. Kufotokozerana uku kuli ndi zinthu ngati izi:
 - A. Mulungu ndi Mzimu Woyera ndipo alibe thupi komanso saoneka ndi maso (Yohani 4:21-24 ndi 1 Timoteo 6:16). Kumbukirani za Fiofane. Kuonekera kwa Mulungu kwa anthu m'njira yomwe anthu akhoza kumvetsetsa. Mulungu akhoza kuonekera m'chinthu kapena kuoneka ngati munthu kapena m'ngelo ndi cholinga chakuti tithe kuona chinthu chomwe tikhoza kuchimvetsetsa (Exsodo 3:2).
 - B. Mulungu ndi munthu kutanthauza kuti ali ndi mzeru ndipo ali ndi makhalidwe ake komanso ubale. Amachita ubale wa padera ndi anthu ake omwe iye anawalenga (Malaki 2:10; Yesaya 43:1,7, 21 ndi Yesaya 44:2, 21,24).
 - C. Mulungu ndi wangwiro. Ndiwolekana ndi zolengedwa zonse chifukwa mwa Iye muli ungwiro opanda malire.. Mwa Iye mulibe tchimo ndi malire, ndipo ndi oposa zolengedwa zonse (Exsodo 15:11, Masalimo 147:5).
 - D. Mulungu ndi ungwiro wake ziri chinthu chimodzi. Mulungu ndi waphumphu. Izi zikutanthauza kuti Iye alibe magawo olekana. Maonekedwe ake ali amodzi. Mwa njira ina Mulungu ndi wa ngwiro mwa Iye yekha monga Iye anazionetsera kwa anthu.
2. Maina amene Mulungu anadzipatsa yekha m'Baibulo alipo ambiri.
 - A. Maina a Mulungu m'Chipangano Chakale
 - i. Elohi, El, kutanthauza kuti ndi wa mphamvu (Genesis 1:1; Deutronomu 10:17).
 - ii. Adonai kutanthauza kuti Mulungu olamulira zinthu zonse (Masalimo 86:8).
 - iii. El-Shaddai kutanthauza kuti ukulu ndi magwero a chitonhozo (Exsodo 6:3).
 - iv. Yehova ndi dzina lopatulika lomwe Ayuda ankatchulira Mulungu ngati wamphavu yonse ndi opanda malire (Exsodo 3:14 & 15).
 - v. Ine ndi Ine (Exsodo 3:14)
 - vi. Mulungu kapena Yahweh (Exsodo 6:3)
 - B. Maina a Chipangano Chatsopano
 - i. Mulungu (Mateyu 1:23)
 - ii. Ambuye (Mateyu 7:21)
 - iii. Atate (1 Akolinto 8:6)
 - iv. Alefa ndi Omega kutanthauza oyamba ndi omaliza (Chibvumbulutso 22:13)
- IV. Maokedwe ndi chikhalidwe cha Mulungu. Mulungu ali ndi maonekedwe ndi chikhalidwe choposa dongosolo lomwe liri pansiri. Pali zikhalidwe zazikulu ziwiri.
 1. Zikhalidwe zomwe ziri mwa Mulungu yekha basi:

Zikhalidwe zimenezi ziri mwa Mulungu yekha ndipo zimaonetsa kusiyana kwakuru komwe kuri pakati pa zolengedwa ndi Mulungu. Zitsanzo za zikhalidwe zimenezi ndi izi:

- A. Mulungu anakhala mwa Iye yekha (Yohani 5:26; Aroma 11:33-36).

- B. Kusasinthika kwa Mulungu zomwe zikutanthauza kuti Mulungu sasintha. Ndi wangwiro (Malaki 3:6).
- C. Kupanda malire kwa Mulungu zomwe zikutanthauza kuti Mulungu alibe malire. Ungwiro wake ulibe malire ndipo sungayezedwe. Iye amapezeka pali ponse, ali wamzeru, wachilungamo, waluntha, wachikondi, ubwino, chiyero ziri zopanda malire (Yobu 11:7-10, Masalimo 145:3). Iye alibe nthawi ndi wamuyaya (Masalimo 90:2; 102:12). Iye ali kumwamba ndi dziko lapansi (1 Mafumu 8:27; Masalimo 139:7-10; Yesaya 66:1 Yereimiya 23:23-24; Machitidwe 17:27-28).
- i. Ungwiro wake ulibe muyeso (Yobu 11:7-11)
 - ii. Umuyaya wake (Masalimo 90:2; Yesaya 41:2)

Izi zikutanthauza kuti Mulungu alibe chiyambi kapena chitsiriziro. Mulungu analipo ndipo alipo. Kodi anthu timazimvetisa bwanji izi? Tikhoza kumvetisa kuti Mulungu ndi anthu alibe chimaliziro koma nkovuta kwambiri kumvetsetsa zoti Mulungu alibe chiyambi. Sitingavetsetse kapena kufotokoza.

- a. Ziripo zinthu zambiri zomwe sitingathe kuzimvetsetsa m’Baibulo zomwe sitingazimvetsetse monga umuyaya ndi utatu wa Mulungu (Deutronomo 29:29) ndi Yesaya 55:8-9) zikufotokoza kuti Mulungu sanafotokoze chiri chonse kwa ife ndipo amaganiza mosiyana ndi ife m’chifukwa chake sitimamvetisa chiri chonse. Tiyenera kuvomereza za umuyaya ndi utatu pokhulupilira basi.
 - iii. Kupezeka kwake paliponse zikutanthauza kuti palibe kumene kulibe Mulungu (Masalimo 139:7-10).
- D. Umulungu wake. Mulungu siogawanika monga thupi ndi Mzimu ndipo sangagawanike. Anthu atatu mu utatu wa Mulungu siwogawanika. Mulungu ndi m’modzi.
2. Zinthu zomwe ziri mwa Mulungu ndiponso munthu. Munthu ali ndi zinthu zimenezi koma ziri ndi malire koma mwa Mulungu ziribe malire. Zitsanzo za zinthu ngati zimenezi ndi:
- A. Tiri ndi chidziwitso chochepa cha zinthu monga sitim’dziwa Mulungu kwathunthu. Mulungu ndi wachidziwitso chonse ndipo izi zikutanthauza kuti Mulungu amadziwa zinthu zonse.
 - B. Nzeru za Mulungu (Aroma 11:33; 1 Akolinto 2:7). Mulungu ndi wanzeru zonse pamene nzeru zathu ziri ndi malire ndipo zimachokera kwa Mulungu (Miyambo 2:6).
 - C. Ubwino wa Mulungu. Mulungu ndi wabwino nthawi zonse. Ubwino uli mwa Iye mwini (Masalimo 100:5, 36:6; 105:21; Mateyu 5:45). Munthu popanda Mulungu ndi woipa. Akhristu ali ndi ubwino omwe umachokera kwa Mulungu, komabe amachimwabe ndipo sachita zabwino monga Mulungu.
 - D. Chikondi cha Mulungu chimaonetsedwa m’njira zambiri (Yohani 3:16 & 17).
- i. Chisomo cha Mulungu chomwe chiri chikondi cha Mulungu chosatiyenera pa ife (Aefeso 1:6-7).

- ii. Chifundo cha Mulungu chimaonetsedwa m'chifundo chake pa ife (Luka 1:54).
- iii. Kupilira kwa Mulungu pa ife (Aroma 2:4).
- E. Chiyero cha Mulungu chikutanthauza kuti Mulungu ndi wangwiro ndi olekana ndi chilengedwe chake (Romans 15:4). Mulungu ndi osiyana ndi chilengedwe chake ndipo ndi okwezeka pamwamba pa zolengedwa zonse m'mphavu zopanda malire (Exsodo 15:11, Yesaya 57:15). Mwa iye mulibe tchimo ndipo munthu ndi okhudzidwa ndi machimo ake (Yobu 34:10; Yesaya 6:5; Habakuku 1:13)
- F. Chilungamo cha Mulungu chimagwirizana ndi chikhalidwe chake. Chilungamo chake ndi ungwiro wake ndi m'mene Iye amakhalira monga woyera. Amayang'anira maulamuliro onse pa dziko lapansi ndi kukhazikitsa lamulo la chilungamo pa munthu, pakupereka mphoto kwa omvera and kulanga osamvera (Masalimo 99:4; Yesaya 33:22; Aroma 1:32).
- i. Chilungamo cha Mulungu (Aroma 1:32). Mulungu anapatsa ife malamulo ake omwe amatsogolera ife pa moyo wathu. Amalonjeza photo kwa omvera ndi chilango kwa osamvera.
- ii. Chilungamo chake chiri m'mphoto zomwe Iye amapatsa anthu ake ndi angelo (Aroma 2:7). Amatipatsa zinthu zabwino chifukwa amatikonda ife.
- iii. Kubwezera kwake kwa chilungamo ndi chilango chomwe iye amapereka kwa ochimwa (Aroma 2:9).
- G. Kukhulupilika kwa Mulungu. Ndi Mulungu woona mwa Iye yekha. Nthawi zonse ndi wokhulupirika. Mulungu sanama (Numeri 23:19).
- H. Uulamuliro wa Mulungu ndi mphamvu zake
 - i. Uulamuliro wa chifuniro cha Mulungu (Daniel 4:35). Mulungu amachita monga Iye amafunira.
 - a. Deutronomo 29:29 akutiiza kuti Mulungu ali ndi chifuniro cha zinsinsi zake komanso chifuniro cha bvumbulutso lake (Aroma 11:33 & 34 akutiiza za chifuniro cha chinsinsi ndipo alinso ndi chifuniro cha bvumbulutso lake (Aroma 12:2).
 - b. Ufulu wa chifuniro cha Mulungu. Mulungu ali ndi ufulu wakulenga ndi kukonda yemwe Iye anfunu (Aroma 9:15:18).
 - c. Chifuniro cha Mulungu pa tchimo. Mulungu amalora kuti tichimwe; koma sakondwera ndi kuchimwa kwathu.
 - ii. Mphamvu ya Mulungu zikutanthauza kuti Mulungu akhoza kuchita zonse zomwe Iye afuna (Yeremiya 32:27) Koma pali zinthu zina zomwe Mulungu sangathe kuchita monga tchimo kapena kusintha. Iye amasunga lonjezo lililonse lomwe Iye analipereka kupyolera m'Baibulo (Numeri 23:19).
- 3. M'chifukwa chiyani tiyenera kuphunzira zikhalidwe ndi maonekedwe a Mulungu?
 - A. Zimatithandiza ife kumvetsetsa za ukulu wa Mulungu pamodzi ndi mphatso ya chipulumutso (Deutronomo 7:21; 10:17).
- 4. Tichite chiyani pa chidziwitso chathu pa Mulungu?

- A. Zikhalidwe za Mulungu zikhale gawo la pemphero lathu. Chiyambi cha pemphero labwino ndi kuuza Mulungu kuti tikum'dziwa Iye; timankonda Iye ndipo tikuthokoza Iye pakuti Iye ayenera kulandira ulemelero. Pemphero loyamika Mulungu chifukwa cha ukulu wake.
- B. Kukondwera mwa Mulungu wankuru

V. Utatu

1. Ife anthu singamumvetsetse Mulungu pakufotokozera za Utatu wake bwino. Kumbukirani kuti tinaphunzira kuti sitingathe kumvetsetsa chirichonse m'Baibulo. Mulungu ndi m'modzi; koma mu umodzi wake muli anthu atatu: Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Apatu sizikutanthauza kuti pali Milingu itau. Ndi munthu m'modzi mwa atatu; ofanana m'thupi, mphamvu ndi ulemelero wao.
- C. Choonadi chimenechi chimatsutsidwa kwambiri ndi anthu azipembedzo za bodza monga Asilamu.
- D. Mukhoza kufufuza Baibulo lonse, simungathe kupeza mau oti Utatu ngakhale kuti chiphunzitso cha Utatu chimaphunzitsidwa m'malo ambiri a m'Baibulo. Chipangano Chakale ndi Chatsopano zimatitsimikizira kuti chiphunzitso cha Utatu ndi choona.
- E. Mavesi a m'Chipangano Chakale omwe amafotokoza za Utatu.
 - i. Mulungu akuzifotokoza yekha mwa *umbiri*, kutanthauza kuti sali munthu m'modzi (Genesis 1:26; 11:7; Yesaya 6:8).
 - ii. Mzimu Woyera akufotokozedwa ngati oima payekha (Yesaya 48:16; 61:1; 63:10).
 - iii. Alipo mavesi ambiri amene amafotokoza za Mzimu (Genesis 1:2; 4:38 1 Samueli 10:6).
- F. Chipangano Chatsopano chimaphunzitsanso za Utatu:
 - i. Utatu unatchulidwa pa nthawi ya ubatizo wa Yesu (Luka 3:21-22).
 - ii. Utatu unatchulidwa pa ulaliki omaliza wa Yesu (Yohani 14:16).
 - iii. Utatu unafotokozedwa pa (Mateyu 28:19).
 - iv. Pa mdalitso wa apositori (2 Akolinto 13:14).
 - v. M'malo ambiri m'buku la (Luka 1:35; 1 Akolinto 12:4-6, 1 Petro 1:2).
2. Atatu ofotozedwa mosiyana.
 - A. Mulungu Atate amatokozedwa m'njira zosiyanasiyana:
 - i. Ngati chiyambi cha zinthu zolengedwa zonse (1 Akolinto 8:6; Aefeso 3:14 & 15; Aheberi 12:9; Yakobo 1:17).
 - ii. Atate wa mtundu wosakhidwa wa ana a Israeli (Deutronomo 32:6; Yesaya 63:16).
 - iii. Atate wa wa okhulupilira monga ana ake a ku uzimu (Mateyu 5:45; Aroma 8:15).
 - iv. Dzina lomwe limagwiritsidwa motsatizana munthu wa chiwiri mu Utatu – Yesu (Yohani 1:14; Yohani 5:17-47).
 - B. Yesu yemwe ali Mwana ndi munthu wa chiwiri mu Utatu.

- i. Ndi wamuyaya zomwe zikutanthauza kuti alibe chiyambi ndi chitsiriziro (Masalimo 2:7 Machitidwe 13:33). Ndi mwana obadwa yekha wa Mulungu
 - ii. Mwana yemwe ali ndi umulungu; ndipo ndi Mulungu (Yohani 1:1; Aroma 9:5). Ali ndi mphamvu zonse za Mulungu.
 - iii. Ntchito zopatsidwa kwa Mwana, Yohani 1:3 akuti zinthu zonse zinalengedwa ndipo zimasamalidwa ndi Mwana. Iye ndiye kuunika kwa anthu onse komwe kuchotsa mdima (Yohani 1:9).
 - iv. Ntchito ya chipulumutso yake imachitika mu umunthu wake, m'amasautso ndi imfa (Aefeso 1:3-14). Ubale wathu wa mtendere umapyolera mwa Yesu (Yohani 14:6).
- C. Mulungu Atate ndi wachitatu mu Utatu.
- i. Maonekedwe a Mzimu Woyera
 - a. Ndi munthu 14:16; 17, 26; Aroma 8:26.
 - b. Ali ndi zinthu zopezeka mwa munthu monga nzeru (Yohani 14:26), ali ndi chikondi (Yesaya 63:19 ndi Aefeso 4:30); Ali ndi chifuniro monga munthu (Machitidwe 16:7).
 - ii. Ubale wa Mzimu Woyera ndi anthu ena mu Utatu (Yohani 15:26, Agalatiya 4:6 akufotokoza kuti amagwirira ntchito limodzi.
 - iii. Mzimu ali ndi ubale ndi anthu ena a mwa Mulungu (1 Akolinto 2:10-11).
 - iv. Nthawi zina timati Yesu kapena Mzimu Woyera ndi yemwe amakhala mwa okhulupilira (Aroma 8:9-10; Agalatiya 2:20).
 - v. Umulungu wa Mzimu Woyera (Machitidwe 5:3-4); Genesis 1:2 ndi Mateyu 28:19 zonse zikuonetsa kuti Mzimu Woyera ndi Mulungu.
 - vi. Pali ntchito zina zomwe zimachitidwa ndi Mzimu Woyera
 - a. (Exsodo 28:3 ndi 1 Samueli 16:13 amawapatsa anthu mphatso za utsogolero pa ntchito zina.
 - b. Amatithandiza kuti timvetsetse Mau a Mulungu, 1 Akolinto 2:13 ndipo anauzira kulembedwa kwa Mau a Mulungu 2 Petro 1:21. Kusowa kwa Mzimu Woyera m'mitima ya osakhulupilira kumapangitsa iwo kusamvetsetsa za Baibulo.
 - c. Ndi gawo la moyo wa m'khristu. Amapereka mphamvu (Machitidwe 1:8). Amatitonthoza ife (Machitidwe 9:31). Amakhala mwa ife (1 Akolinto 9:13). Mzimu Woyera ndi mphatso ya Mulungu yomwe amatithandiza ife kudutsa m'moyo wamasautso uno.
 - d. Mzimu Woyera ndi amene amatengetera akhristu ku chiombolo (Tito 3:5).
- VI. Ntchito za Mulungu
1. Zinthu zosasinthika za Mulungu ndi zikonzero kapena cholinga zomwe mu ulemelero wake anakhazikitsa zonse zomwe zimachitika. Tinganenenso kuti, Mulungu anali ndipo ali ndi chikonzero cha zonse zomwe zikuchitika. Onani maumboni a Chipangano Chakale monga Yesaya 46:10; Yobu 23:13; 14, Genesis 50:20).
 2. Maonekedwe a zinthu zosasinthika za Umulungu
 - A. Ziri mu nzeru za Mulungu (Aefeso 1:11)
 - B. Chifuniro cha Mulungu chimachitika (Miyambo ndi Yesaya 46:10).
 - C. Sasintha chifuniro chake (Yobu 23:13-14). Mulungu ali yemweyo dzulo, lero ndi mawa.
 - D. Chifuniro chake sichifuna zinthu zina kwa ife (Aefeso 2:8)

3. Zinthu zosasinthika za Mulungu

- A. Chisankho cha nthawi zosayamba (Machitidwe 4:28; Yuda 4; Aefeso 1-4).
- B. Chilengedwe chinali chinthu chosasinthika cha Mulungu chomwe Iye analenga dziko lapansi ndi zonse ziri m'momwe (Genesis 1:2).
 - i. Nthawi ya kulengedwa kwa dziko ndiyo chiyambi cha nthawi (Genesis 1:1).
 - ii. Mulungu analenga pakulankhula ndipo zinthu zonse zinalengedwa poponda kanthu (Masalimo 33:9; Aheberi 11:3).
- C. Mulungu analenganso zinthu zosaoneka komanso dziko la mizimu komwe kumakhala angelo, Serafini ndi Akerubi (Yesaya 37:16).
 - i. Maonekdwe angelo. Ali ndi anzeru (2 Samueli 14:20). Ali ndi chikhalidwe chabwino komanso choipa (Yuda 1:6; Chibvumbulutso 14:10). Ndi zolengedwa za uzimu (Machitidwe 19:12).
 - ii. Undindo wa angelo
 - a. Akerubi ali ndi ntchito yomwe timaona m'mau a Mulungu (Genesis 3:24, Exsodo 25:18; 2 Samueli 22:11).
 - b. Aserafini alinso ndi maudio omwe timaona m'mawu a Mulungu (Yesaya 6:2; 3, 6).
 - iii. Ntchito za angelo abwino ndi izi:
 - a. Iwo amayamika Mulungu usiku ndi usana (Yesaya 6; Chibvumbulutso 5:11; Masalimo 103:20)
 - b. Amatumikira Mulungu (Aheberi 1:14).
 - c. Amakondwera pa chipulumutso cha ochimwa (Luka 15:10).
 - d. Amapereka madalitso ochokera kwa Mulungu (Machitidwe 5:19).
 - e. Amapereka chilango (Genesis 19:1 & 13).
 - iv. Ntchito za angelo omwe anagwa pamaso pa Mulungu
 - a. Awa ndi angelo amene analengedwa angwiro, koma anasakha kuukira Mulungu (2 Petro ndi Jude 1:6) akufotokoza za izi. Angelo oipa amenewa amachita chirichonse chotsutsana ndi Mulungu ndi anthu ake.
 - b. Satana ndi mtsogoleri wa angelo onse oipa (Mateyu 25:41). Iye ndiye gwero la machimo onse (Yohani 8:44). Angelo oipa amenewa ndi a mphavu (Yuda 1:9).
- 4. Zonse ndi gawo la dziko lapansi lomwe ife timakhalamo.
 - A. Nkhani ya chilengedwe ikupezeka pa Gensesis 1.
- 5. Chisamaliro cha Mulungu. Izi zikutanthauza kuti Mulungu amalamulira zinthu zonse zolengedwa. Iye amalamula zonse zolengedwa. Sitidalira pa mwayi, komatu pa Mulungu (Mateyu 6:25-34). Mulungu akulamulira chilengedwe chake. Iye akulamulira zonse zimene zikuchitika. Ndipo palibe chimachitika kunjira kwa chifuniro chake (Mateyu 10:29, Machitidwe 2:23, Yesaya 45:7).
 - A. Chisamaliro cha Mulungu ndi ntchito ya chiyero, nzeru ndi m'mphamvu zake zomwe amasamalira zonse za chilengedwe ndi zochita zache Mulungu akupitiriza kusamalira zinthu zonse pa chilengedwe chake (Masalimo 136:25; Nehemiah 9:6; Machitidwe 17:28 ndi Akolose 1:17). Mulungu amalamulira pa china chirichonse chochitika panso pano.
 - B. Magawo atatu a chisamaliro:

- i. Chisamaliro cha Mulungu ndi ntchito ya Mulungu yomwe Iye amasamalira dziko lonse. Izi zikuonetsa kuti pamene Mulungu amapanga zinthu zake mwa Iye yekha, koma munthu amadalira pa Mulungu basi (Masalimo 63:8).
- ii. Kuchitika kwa zinthu mwadongolo ndi ntchito ya Mulungu yomwe imachitika mogwirizana ndi chilengedwe chake pamene zolengedwa zimachita zinthu molondora ndi mosasemphanitsa. Chilengedwe ndi anthu sizingachite zinthu mwa izo zokha popanda Mulungu ngakhale pamene munthu akuchimwa. Palibe munthu akhoza kuchita zabwino kapena zoipa popanda mphamvu ya Mulungu. Izi sizikutanthauza kuti Mulungu ndi amene amatipangitsa ife kuti tichimwe. Tiri ndi ndi udindo wosachita zochimwa (Deutronomo 30:19), koma Genesis 6:5 akutiphunzitsa kuti munthu nthawi zonse amasankha kuchimwa. Timatha kuchita zabwino pokhapokha Mulungu akakhala mwa ife kuti tichite zabwino (Aroma 6:1, 11, 22).
 - a. Mulungu amalamulira zinthu zina zoipa kuti zichitike (Genesis 45:5 ndi 50:20)
 - b. Mulungu amateteza ntchito za anthu ochimwa (Yobu 1:12).
 - c. Amagonjetsa zoipa kuchitira ubwino zinthu zina (Genesis 50:20)
- iii. Ulamuliro wa Mulungu ndi ulamuliro opitilira wa Mulungu pachina chirichonse kuti zinthu zonse zikachitike molingana ndi chifuniro chake. M’Baibulo timaphunzira kuti Mulungu ndi Mfumu yakumwamba ndipo amalamulira pa china chirichonse monga Iye afunira (Masalimo 22:28, Yesaya 33:22).

VII. Chiphunzitso cha munthu mogwirizana ndi Mulungu

1. Munthu asanachimwe
 - A. Magawo atatu a munthu
 - i. Munthu ali ndi magawo awiri (thupi ndi mzimu) - Mateyu 10:28 kapena 1 Akolinto 5:3 ndi 5.
 - B. Munthu monga chifanizo cha Mulungu
 - i. Mulungu analenga munthu m’chifanizo cha chilengedwe chake. Munthu ndi yekhayo amene analengedwa m’chifanizo cha Mulungu (Genesis 1:26-27).
 - C. Kodi chifanizo cha Mulungu zikutanthauza chiyani?
 - i. Munthu ndi mzimu, ali ndi nzeru, khalidwe ndipo ndi osafa. Akhoza kukhala ndi ubale ndi Mulungu. Munthu ndi fanizo leni leni la Mulungu. Koma izi mulibe mwa nyama 9Genesis 9:6, Yakobo 3:9).
2. Munthu ndi Chipangano cha ntchito
 - A. Mulungu anapanga pangano ndi munthu lomwe limafuna munthuyo kuti amvere Mulungu (Genesis 2:16-17). Moyo osantha uli mpangano lomvera (Aroma 10:5; Agalatiya 3:12).
3. Magawo a Pangano la ntchito

- A. Mulungu anapatsa munthu, monga choimira mwa Adamu, madalitso a moyo wosatha ndi chimwemwe changwiro. Koma zimafunikira kuti munthu amvere kwa thunthu.
 - B. Malonjezo a pangano. Lonjezo ndi moyo wosatha, moyo okhala m'chiyero.
 - C. Zoyenera mpangano ndi kupitilira kokhala moyo womvera.
 - D. Chilango cha pangano pakusamvera kulangidwa m'thupi, m'moyo wa uzimu ndi imfa yamuyaya.
4. Kuyenera kwa chipangano cha ntchito
- A. Mulungu amafunabe ife kumvera malamulo ake (Levitiko 18:5 ndi Agalatiya 3:12); koma chigwereni munthu mu uchimo, palibe munthu akhoza kusunga lamulo mwa ngwiro.
 - B. Pakadali pano udindo womvera lamulo umakwaniritsidwa ndi Mpulumutsi Yesu. Sitingapeze moyo osatha chifukwa cha kumvera lamulo. Tikhoza kupeza chipulumutso kupyolera chikhulupiliro mwa Yesu Khristu. Kumvera kwake kwa ngwiro kumatipanga ife kulandira moyo osatha (Aheberi 11:6).
5. Munthu ndi ochimwa
- A. Tchimo la munthu chifukwa cha kugwa kwake. Baibulo likutiphunzitsa kuti muzu wa zoipa zonse uri m'tchimo loyamba la Adamu (Genesis 3:6).
 - B. Tchimo loyamba linadza chifukwa chakusamvera Mulungu. Kusamvera kwao kunali kudya chipatso choletsedwa. Kudya kwao kunali kusamvera Mulungu. Munthu anakana kulora Mulungu kulumulira moyo wake. Uku kunali kunyada ndi kufuna kufanana ndi Mulungu.
 - C. Anagwa mu uchimo pamene iwo anayesedwa ndi njoka. Satana anagwiritsa njoka monga tikuona pa Yohani 8:44 kuti anthu anagwiritsidwa ntchito ndi Satana. Lero lino anthu ambiri amagwiritsidwa ntchito ndi Satana. Akhristu sitiyenera kugwiritsidwa ntchito ndi Satana.
 - D. Zotsatira za tchimo loyamba. Zinthu zonse zoipa za dziko lapansi zinatigwera. Munthu anataya chidziwitso choona cha Mulungu, Chilungamo ndi chiyero. Munthu anachimwiratu, ndipo nthawi zonse amachita zinthu zonyansa.
6. Maonekedwe a tchimo
- A. Timafotokoza kuti tchimo ndi china chirichonse chimene timalankhula, kuchita, kapena kuganiza zomwe zimaipira Mulungu. Ndichina chirichonse chimene sitichinena, sitichichita ngakhale kuchiganizira choipira Mulungu (Genesis 2:17-18). Koteri timachimwa pochita kapena kusachita.
 - B. Luka 11:23 akuti palibe kusatenga nawo gawo, pakutero mumakhala mbali ya Mulungu kapena yotsutsa Mulungu.
 - C. Munthu aliyense amabadwa ndi tchimo (Yeremiya 17:9).
 - D. Machimo athu amatipanga ife kuchimwa ndi kukhala pansu pa mkwiyo wa Mulungu (Aroma 1:18, 3:23; 6:23).
 - E. Aliyense ndi ochimwa (1 Mafumu 8:46). Aliyense ndi okhudzidwa ndi tchimo.

VIII. Pangano la chisomo kapena pangano la chiombolo

1. Mawu oti pangano amatanthauza kuti m'gwirizano wa anthu awiri kapena magulu awiri. Mulungu anapanga mapangano ambiri ndi anthu.
 2. Tiyenera kusiyanita pakati pa mapangano awiriwa omwe ndi ofanana ndipo sitimawamvetsetsa bwino. Pangano la chiombolo ndi pangano la chisomo.
- A. Pangano la chiombolo limati chipulumutso chathu chinali m'malingaliro a Mulungu ndipo chikonzero cha chiombolo chinali mu ulamuliro wosasinthika wa Mulungu (Aefeso 1:4; 3:11; 2 Timoteo 1:9; Yohani 5:30; 43; 6:38-40; 17:4-12).
- i. Pangano ndi m'gwirizano wa pakati pa Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera. Munthu sanatenge nao gao mpangano limeneri.
 - ii. Pangano la chiombolo. Mulungu Atate anafuna Mwana kukhala ngati munthu opanda tchimo m'moyo wake ngakhale limodzi (Agalatiya 4:4 & Aheberi 4:15). Mulungu Atate analonjeza kuthandiza Mwana pa ntchito yake.
 - iii. Mwana anapereka dipo la tchimo la machimo anthu kuti tikhale ndi moyo osatha (Yohani 10:11 ndi Agalatiya 1:4).
 - iv. Pangano iri sirikufuna ntchito ina iriyonse kwa ife koma likufuna ife kumvera bvumbulutso la chifuniro cha Mulungu. Izi zikutanthauza kuti timavomereza malonjezo a Panganoli ndi chikhulupiliro (Aefeso 2:8).
 - v. Mulungu Atate analonjeza kuti adzatumiza Mzimu Woyera kuti upange izi:
 - a. Kupanga thupi lake la uzimu (Mpingo) pobadwanso mwatsopano ndi kuyetsedwa, kuti Mzimu Woyera, utiphunzitse, utitsogolere ndi kuteteza mpingo (Yohani 14:26; 15:26; 16:13, 14).
 - b. Mzimu Woyera umathandizira kuti Yesu Khristu alandire anthu onse opatsidwa kwa Iye (Yohani 6:37, 40, 44, 45).
 - c. Makamu a wanthu adzapatsidwa kwa Khristu kupanga ufumu wake (Masalimo 22:27; 72:17).
- B. Pangano la Chisomo. Pangano la Chisomo ndi lofanana ndi pangano la chiombolo, ndipo limafotokozedwa kuti ndi pangano la pakati pa Mulungu ndi osankhidwa ochimwa omwe Mulungu mwini amampatsa Iye (Yesu) pamodzi ndi madalitso a chipulumutso kwa osankhidwa ochimwa, ndipo ochimwa amavomereza Mulungu pamodzi ndi mphatso zonse za chisomo ndi chikhulupiliro (Deutronomo 7:9; 2 Mbiri 6:14; Masalimo 25:10,14; 103:17, 18).
- i. Malonjezo ndi zofunikira za pangano la Chisomo
 - a. Mulungu amalonjeza kukhala Mulungu wathu ndipo timakhala anthu ake m'moyo uno ndi kunthawi zosantha (Yeremiya 31:33, Tito 3:7; Aheberi 11:7; Yakobo 2:5).
 - b. Tiri ndi udindo ovomereza panganoli ndi chikhulupiliro, ndipo tikuyenera kudzikhuthura tokha kwa Mulungu pakumvera.
 - ii. Maonekedwe a Pangano
 - a. Ndi losatha ndipo ndi losasinthika. Lidzakhala kunthawi zosatha (Aheberi 13:20).
 - b. Ndi pangano la okhulupilira okha Ayuda ndi amitundu onse.

- c. Panganolo ndi lofanana m'Chipangano Chakale ndi Chatsopano (Genesis 3:15, Agalatiya 3:8). M'khalapakati wathu ndi Khristu (Aheberi 13:8; Machitidwe 4:12).
- IX. Chiphunzitso cha munthu ndi ntchito ya Khristu (chiphunzitso cha Khristu)
1. Maina a Khristu
 - A. Awa ndi maina ofunikira kwambiri a Khristu.
 - i. Yesu – dzinali tanthauzo lake limafanana ndi dzina loti Yoswa 1:1; Zakaliya 3:1; Ezara 2:2). Yesu ndi mau a Chiheberi kutanthauza kupulumusta, koto dzinali limatanthauza kuti Iye ndi Mpulumutsi (Mateyu 1:21).
 - ii. Yesu amatchedwa Khristu m'Chipangano Chatsopano ndipo Mesiya m'Chipangano Chakale kutanthauza kuti odzodzedwa. Onani (Machitidwe 4:27 ndi 10:38) pamene Iye akutchuridwa odzodzedwa.
 - iii. Mwana wa Munthu. Irinso ndi dzina la Khristu monganso likunenedwa m'buku la Daniel 7:13. Dzinali limasonyeza umunthu wa Yesu komanso kubwera kwake m'mitambo m'tsogolo mu ulemelero ndi m'mphavu (Mateyu 16:27; 28:64; Luka 21:27).
 - iv. Mwana wa Mulungu. Khristu amatchedwa mwana wa Mulungu chifukwa cha zinthu izi: Iye ali wachiwiri mu Utatu wa Mulungu. Iye ndi Mulungu ndipo Iye anabadwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera (Luka 1:35; Mateyu 11:27).
 - v. Ambuye Yesu. Ophunzira ake ankamutchura Iye motero pomupatsa ulemu ndipo ndime zina za Baibulo zimatanthauza kuti Khristu ndi Mwini wa mpingo (Aroma 1:7; Aefeso 1:17).
 2. Chikhalidwe cha Khristu. Mau a Mulungu akuti Khristu ndi munthu yemwe ali ndi magawo awiri, munthu komanso Mulungu; Iye ndi munthu weni weni komanso Mulungu weni weni. Mau a Mulungu amene akutanthauza kuti Iye anali Mulungu weni ndi Mateyu 16:16; Yohani 1:1.
 - A. Yesu waku Nazareti anali Mulungu; izi zikutanthauza kuti Iye analipo asanabadwe ngati Yesu waku Nazareti; Khristu anatenga nao gawo pakulengedwa kwa dziko ndi miyamba (Yohani 1:1). Mukudzikhuthura kwake; tikuona kudzichepetsa kwake pamene Mulungu anasiya mphamvu ndi ulemelero wake wolamulira dziko ndi zonse ziri m'mwemo pakutenga thupi la ukapolo (Yohani 1:14; 1 Yohani 4:2. M'mau ena, Yesu anali Mulungu ndipo kuti atipulumutse anasiya ulemelero wakumwamba, nabadwa ngati munthu nakhala pakati pa anthu.
 - B. Pamene pali kudzichepetsa sitingasiye kukwezeka kwa Khristu. “Kukwezeka kwa Khristu” kukuoneka pakuuka kwake kwa akufa pa tsiku lachitatu; kukwera kwake kumwamba; kukhala kwake kudzanja la manja la Mulungu Atate; komanso kudza kwake mu ulemelero kuweruza dziko lapansi pa tsiku lomaliza (1 AKolinto 15:4; Mariko 16:19; Machitidwe 17:31).
 - C. Yesu analinso munthu. Tikuona kuti Mulungu anazionetsa yekha m'thupi (1 Timoteo 3:16). Ndime zina za m'Baibulo zimene zimafotokoza za umunthu wake

ndi Yohani 8:40; Machitidwe 2:22; Aroma 5:15). Ngati munthu Yesu anakumana ndi zonse zimene munthu amakumana nazo monga kuyesedwa, kudwala, njala chisoni etc. Komatu sanachimwe.

- D. Magawo awiri achikhalidwe chake ali olumikizana mwa munthu m'modzi. Izi zikutanthauza kuti pamene Khristu ali ndi thupi la umunthu, komatu simunthu. Iye ali Mwana wosasinthika wa Mulungu. Pakuzikhuthura kwake sanasinthe kukhala munthu, anangodzichepetsa podziphatikiza ku umulungu ndi umunthu wake.
- i. Izi zikutanthauza kuti Iye ndi munthu komanso Mulungu pakukhala ndi zonse zomwe ziri ndi Mulungu komanso munthu. Iye ndi Mulungu munthu. Izi ndi zovuta kuzimvetsetsa, komatu ndi zimene Mau a Mulungu akutitsimikizira (Yohani 10:30; 17:5). Sitingamvetsetse m'mene Iye anakhalira Mulungu komanso munthu pa nthawi imodzi, komatu ichi ndi chiphunzitso chopambana kwambiri ndipo tiyenera kuchivomereza kuti tikhale akhristu.
3. Kumvera kwa Khristu. Tikugwiritsa ntchito mau oti “kumvera” pofuna kufotokoza za ubale wa Yesu ku lamulo.
- A. Tikati kudzichepetsa tikutanthauza kuti Khristu anasiya ulemelero wake wa umulungu omwe Iye anali olamulira wa zinthu zonse pakukhala munthu monga kapolo. Tinenenso kuti Yesu amene anapanga lamulo anakhala panso pa lamulo pakudzichepetsa kwake.
- i. Kudzikhuthura ndi kubadwa kwa Khristu. Tikudziwa kuti Iye anabadwa mwa mkazi, Maliya yemwe anampatsa Iye thupi la umunthu (Yesaya 7:14; Mateyu 1:20-21). Kubadwa kodabwitsaku kunachitika chifukwa cha mphamvu ya Mzimu Woyera, ndipo izi zinachitika kamodzi kokha chilengedwere dziko lapansi. Zomwe zikutanthauza kuti Yesu anabadwa opanda tchimo lomwe anthu tonse timalirandira kuchokera kwa Adamu (Luka 1:34-38).
 - ii. Masautso a Khristu sanali popapachikidwa pa mtanda pokha. Moyo wake onse unali wamasautso. Anakanidwa. Adani ake ananzuza Iye. Anayesedwa ndi Satana mdyerekezi, anazunzika ndi machimo adziko lapansi ndipo analemedwa ndi katundu wa machimo omwe anakhala pa Iye (Yesaya 53:3) akufotokoza zimenezi.
 - iii. Imfa ya Khristu ndi imfa ya moyo wake yomwe inadza chifukwa choweruzidwa (Yesaya 53:3). Imfa ya pamtanda ndi imfa ya temberero chifukwa chakusenza machimo athu (Deutronomo 21:23; Agalatiya 3:13).
 - iv. Kuikidwa kwake ndi gawo lina lakudzichepetsa kwake chifukwa kubwerera kwathu ku dothi ndi gawo la temberero (Genesis 3:19).
- B. Kukwezeka kwake kwa Khristu kunali kwa kuti Iye sanali panso pa chilango cha tchimo. Iye anakwera kumwamba kumene Iye anavekedwa ulemelero ndi ulemu.

Kumene Iye anabwerezetsedwa ulemerero onse ndi ulemu wakumpanga Iye kukhala Mulungu.

C. Pali magawo anayi akukwezeka kwake:

- i. Kuuka kwa akufa ndi gawo loyamba. Izi zikutanthauza kuti Yesu anakhalanso ndi Moyo. Thupi ndi mzimu wake zinabwerezedwanso kukongola ndi mphamvu zake kuposa kale. Iye anali osiyana ndi ena amene anawukapo kale; Iye sanaukitsidwe chifukwa anauka ndi thupi la uzimu (1 Akolinto 15:44-45). M'chifukwa chake Iye amatchedwanso oyamba obadwa wa iwo ogona (1 Akolinto 15:20). Iye amatchedwanso oyamba obadwa wa akufa. Ndipo izi ndi zovuta kuzimvetsa koma chofunikira kwambiri kukumbukira ndi chakuti kupyolera kukuwukitsidwa kwake Iye anakhala wopereka mzimu wopatsa moyo (1 Akolinto 15:46). Kuwukitsidwa kwa Khristu ndi chinthu chozizwitsa chomwe chikutsutsana ndi m'mene zimakhallira pachilengedwe ndipo ndi chinthu chopambana kwambiri choti tichikhulupilire. Chiukitso chiri ndi magawo atatu opambana:
 - a. Mulungu Atate anakhutitsidwa ndi ntchito za lamulo zokwaniritsidwa mwa Khristu.
 - b. Zimasonyeza zomwe zidzachikira akristu onse (Aroma 6:4-5) ndi Atesolonika 4:14).
 - c. Ndi maziko akulungamitsidwa, kubadwanso mwatsopano ndi chiukitso chotsiriza (Aroma 4:25; 1 Petro 1:3).
- ii. Gawo lachiwiri lakukwezeka kwake ndi kukwera kumwamba monga Iye anakwera chomwe kuli kumalizitsa chiukitso. Ndi chitsimikizo cha ife cha malo athu kumwamba (Aefeso 2:6).
 - a. Kukwera kwake kumwamba kunapangitsa Iye kukhala kudzanja la manja la Mulungu chomwe chikusonyeza mphamvu ndi ulemelero (Aefeso 1:20; Aheberi 10:12).
- iii. Kukhala kwake ku dzanja la manja la Mulungu ndi kuzimbaitsa kuti Yesu ali pamalo a mphamvu ndi ulemerero, pamene Iye akulamulira ndi kuteteza mpingo, kulumulira chilengedwe ndi kupempherera anthu ake.
- iv. Kukwezeka kwa Khristu kudzafika pa chimake pamene Iye adzabweranso kuweruza amoyo ndi akufa (Machitidwe 1:11; Chibvumbulutso 1:7).

Chidule ndi kuunikanso

1. Kuzichepetsa kwa Khristu kukupezeka pa Agalatiya 3:13; Agalatiya 4:4-5; Afilipi 2:6-8).
2. Kuzikhuthura kukupezeka pa Yohani 1:14; Aroma 8:3).
3. Kubadwa mwa namwali kukupezeka pa (Yesaya 7:14; Luka 1:35).
4. Kuukitsidwa kukupezeka pa (Aroma 4:25; 1 Akolinto 15:20)
5. Kukwera kumwamba kukupezeka pa (Luka 24:51; Machitidwe 1:11).
6. Kubweranso kwake kukupezeka pa (Machitidwe 1:11; Chibvumbulutso 1:7).

4. Ntchito za Khristu

- A. Maudindo a Khristu. Baibulo limafotokoza kuti Yesu ali ndi maudindo atatu; m'neneri, wansembe ndi mfumu.
- i. Chipangano Chakale chinanenera za kubwera kwake monga m'neneri (Deutronomo 18:15) zomwe tikuona kuti zikuchitika pa (Machitidwe 3:22-23).
 - a. Yesu ananena za Iye yekha monga mneneri (Luka 13:33).
 - b. Anafotokoza zinthu za mtsogolo (Mateyu 24:3-35; Luka 19:41-44).
- B. Chipangano Chakale chinaneneranso za kubwera kwake monga wansembe (Masalimo 110:4; Zakaliya 6:13).
- i. Iye akutchedwa wansembe wankulu (Aheberi 3:1; 4:14; 5:5; 6:20; 7:26; 8:1).
 - ii. Iye akufotokozedwa monga wansembe ochotsa machimo anthu (Yohani 1:29; Aroma 3:24).
 - iii. Ntchito ya Khristu monga wa nsembe, poyamba kupereka nsembe ya uchimo pa machimo athu. Nsembe za Chipangano Chakale zinkalozera nsembe yaikulu ya mtsogolo (Aheberi 9:24; 13:11-12).
 - a. Monga nsembe yathu, akutchuridwa Mwana wa Nkhosa (Yohani 1:29).
 - b. Monga nsembe yathu, akutchuridwa Pasaka yathu (1 Akolinto 5:7).
 - c. Monga wansembe wankulu, Khristu amatipembedzera ife. Iye ndi Kazembe wathu wotipembedzera m'malo mwathu. Mwachitsanzo Khristu amatipembedzera kwa Atate kuti tikapindure mwa Iye (1 Yohani 2:2; Aroma 8:34).
 - d. Izi zikutanthauza kuti amapereka nsembe yake kwa Mulungu ndipo Iye amapereka madalitso ake auzimu kwa anthu ake chifukwa cha nsembe yake (Yohani 17:9; 20).
- C. Chipangano Chakale chinanenera za kubwera kwake monga Mfumu.
- i. Akufotokozedwa monga mfumu ya uzimu ya mpingo. Baibulo limafotokoza zimenezi m'malo ambiri (Mika 5:2; Zakaliya 6:13; Luka 1:33; Yohani 18:36).
 - ii. Iyenso ndi mfumu ya zonse zolengedwa. Amatilamulira ife (Mateyu 28:18) akufotokoza kuti ulamuliro onse kumwamba ndi dziko lapansi zapatsidwa kwa Ine.
 - a. Ufumu wake monga mkhalapakati wa mpingo. Iye ali ngati mfumu monga olamulira zochitikira anthu onse ndi mayiko. Iye akulamulira moyo wa dziko ndiku pangitsa ilo kumvera kucholinga cha chiombolo chake ndikuteteza mpingo wake ku zoopsa za dziko lapansi. Dziko lapansi lidzatha pamene adani onse a Ufumu wa Mulungu adzagonjetsedwa.
 - b. Pa nthawi imeneyi ufumu udzabwezeretsedwa kwa Atate (1 Akolinto 15:24-28).
5. Dipo lopyolera mwa Khristu. Dipo likutanthauza kuti kuyanjanitsidwa ndi Mulungu. Tisanakhale akhristu tinali adani a Mulungu; koma nsembe ya Yesu Khristu inapangitsa ife kukhala pa chiyanjano ndi mtendere ndi Mulungu. Pakutero tinayanjanitsidwa kwa Mulungu ndipo mkwiyo wake unachotsedwa pa ife kupyolera m'nsembe ya Yesu.

A. Kufunika kwa dipo la nsembe ya Khristu

- i. Limakondweretsa Mulungu (Yesaya 53:10; Aefeso 1:6-9).
- ii. Ndi lokhazikika m'chikondi cha Mulungu (Yohani 3:16)
- iii. Baibulo limatiphunzitsa kuti Mulungu ndi wangwiro ndi woyera salekelera tchimo, ndipo amatsutsana nalo (Exsodo 20:5; Aroma 1:18).
- iv. Mulungu anaika chilango cha imfa pa anthu onse ochimwa (Genesis 3:3; Aroma 6:23) Ndipo njira yokhayo imene Mulungu akhoza kutipulumutsa ndi kupyolera m'dipo la nsembe Yesu osachimwayo.

B. Chikhalidwe cha dipo

- i. Linakwaniritsa chilungamo cha Mulungu. Cholinga choyamba chenicheni cha dipo ndi kuyanjanitsa Mulungu kwa ochimwa. Chachiwiri ndi kuyanjanitsa ochimwa kwa Mulungu.
- ii. Linali dipo losasinthika. Kusasinthika zikutanthauza kuti linali mulom'malo. Mulungu analandira nsembe ya Yesu m'malo mwathu. Tinganenenso kuti, Khristu analangidwa chifukwa cha machimo athu m'malo moti tikalangidwe ku Gehena ku nthawi zosantha. Izi zinachitika chifukwa choti Mulungu analandira dipo losasinthika m'malo mwathu.
 - a. Chipangano Chakale ndi chimene chinayamba kuphunzitsa za kufunika kwa ntchito ya dipo la Khristu. Linafunika kukhala la mwazi (Levitiko 1:4; 17:11).
 - b. Timaphunzira kuti machimo athu anaikidwa pa Khristu (Yesaya 53:6).
 - c. Khristu anasenza chilango cha mkwiyo wa machimo athu (Yohani 1:29) ndipo anapereka moyo wake kwa ochimwa (Agalatiya 1:4).

C. Dipo linkafunikira ntchito yochitidwa ndi yosachitidwa ya kumvera kwa Khristu. Kuchitika ndi kusachitika kwakumvera kwa Khristu pamodzi sikungalekanitsidwe.

- i. Kuchitika kwakumvera kwa Khristu kumakhudza zonse zimene Yesu anachita pakumvera lamulo m'malo mwa ochimwa kuti Iye alandire moyo osatha wa iwo. Zitsanzo za zochitika za kumvera:
 - a. Yesu anali kumvera malamulo onse kuti Iye alandire moyo osatha wa anthu ake.
 - b. Iye anali kumvera pakulora kunzuzika ndi imfa (Yohani 10:18).
- ii. Kumvera kwa kusachita kukutanthauza zonse zimene Yesu anasautsidwa chifukwa cha ife. Zitsanzo zakumvera kwa kusachita:
 - a. Iye analora kusautsidwa ndipo anapereka dipo la machimo athu. Iye anavomereza.
 - b. Iye analora pakumvera lamulo.
- iii. Pamene tikusiyanitsa masautso awiri; dziwani kuti sitingathe kuwasiyanitsa iwo.
- iv. Tinene kuti kupyolera kumvera kwakusachita kwake Iye anapereka dipo la machimo athu pakuchotsa tembelero pa munthu, Iye anapambana moyo osatha kwa ochimwa.
- v. Kupyolera kumvera kwake kwa kuchita, Iye anapambana moyo wosanthanso kwa ochimwa (Agalatiya 4:4-5).

- D. Pamene dipo ndi lokwanira kwa anthu onse, komatu sionse amene ali opulumutsidwa. Tikudziwa kuti sionse amene adzapite kumwamba.
- i. Khristu anapereka moyo wake chifukwa cha ochimwa (Mateyu 1:21).
 - ii. Anafera nkhusa zake (10:11).
 - iii. Anafera mpingo wake (Machitidwe 20:28).
- X. Chiphunzitsa cha ntchito ya Mzimu Woyera - chisomo chaulere chawamba
1. Chisomo chaulere chawamba ndi ntchito ya Mzimu Woyera m'mitima ya anthu onse pamodzi ndi ochimwa omwe.
 - A. Kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera kumathandizira kutibweza ku tchimo pofuna kukhazikitsa bata pakati pa anthu. Izi zikutanthauza kuti Mzimu Woyera umatha kupanga anthu kusakhala ndi makhalidwe oipa monga iwo akhoza kutero popanda kutsogozedwa ndi mphamvu yapadera ya Mzimu Woyera.
 - B. Chisomo chaulere chawamba ndi madalitso wamba omwe Mulungu amapereka kwa anthu posankha monga chuma, mvula etc. Pamene imfa ya Khristu sidzapulumutsa wina aliyense, kapena mtundu wonse wa anthu sudzapindura ndi imfa yake. Kukanakhala kuti kulibe chisomo chaulere chawamba pa anthu onse padziko lapansi moyo ukanakhala woopsa kwambiri. Zitsanzo:
 - i. Moyo wathu ulipo chifukwa chachisomo chawamba. Chilango cha imfa pa munthu chifukwa cha tchimo chinachedwetsedwa. Mulungu anampatsa munthu mpata wolapa (2 Petro 3:9).
 - ii. Zinthu zoipa zimalephera kuchitika chifukwa cha chisomo cha chisomo chawamba. Mwachitsanzo malamulo a wanthu amathandizira kuletsa zoipa zina. Maganizo a wanthu amathandiza kuletsa zoipa. Izi zimathandizira kuchepetsa chionengeko chomwe tchimo likhoza kubweretsa pakati pa anthu (Genesis 20:6; Yobu 2:6).
 - iii. Anthu tonse tiri ndi choonadi ndi chikhalidwe chabwino. Anthu onse ali ndi maganizo abwino m'mitima yawo. Aliyense amafuna choonadi, makhalidwe abwino komanso kupembedza (Aroma 2:14-15; Machitidwe 27:22).
 - iv. Chisomo chawamba chaulere chimatipanga kukhala ndi ntchito zabwino. Munthu osapululumutsidwa amathanso kuchita ntchito zabwino ngakhale kuti iye alibe chikhulupiliro mwa Yesu Khristu (2 Mafumu 1:29-30; Luka 6:33).
 - v. Chisomo chaulere chimabweretsa madalitso achilengedwe monga Mvula pa mbewu zathu. Anthu onse amalandira madalitso osatiyenera kuchokera kwa Mulungu (Masalimo 154:9; Machitidwe 14:16-17).
 - XI. Maitanidwe ndi kubadwanso mwatsopano. Tanthauzo la maitanidwe ndi kuitanidwa kapena kupemphedwa kuti upite kumalo kwina monga kwa Yesu.
 1. Maitanidwe ndi m'mene anthu amapemphedwera kuti adze kwa Yesu Khristu (1 Akolinto 1:9).
 - A. Maitanidwe akunja ndi kuperekedwa kwa Yesu kwa ochimwa pakupemphedwa kuti avomere Khristu m'chikhulupiliro kuti alandire chikhululukiro cha machimo awo ndi

moyo osatha. Maitanidwe Amachitika pakumva Mau a Mulungu kupyolera m'Baibulo polalikira kapena kuphunzitsa. Komanso ngakhale pakuwereka Baibulo. Maitanidwe akunja amakhala ndi:

- i. Kupereka mfundo za uthenga wabwino (Mateyu 28:19)
 - ii. Kupemphedwa kulapa ndi kukhulupilira Yesu Khristu (Maliko 1:15)
 - iii. Lonjezo la chikhulupiliro ndi chipulumutso (Luka 1:77).
 - iv. Maitanidwe kuti achitike amasoweka chikhulupiliro ndi kulapa. Maitanidwe ndiko kuitana kwa Mulungu ndipo Iye ali okhulupilika (Numeri 23:19).
 - v. Maitanidwe akunja amachitika kwa anthu onse kwa amene uthenga ukulalikidwa (Yesaya 45:22).
 - vi. Ngati munthu savomera maitanidwe a Mulungu atamva kuitanidwe, amakhala ochimwa kwambiri kulekana ndi amene sanamvepo maitanidwe. Chifukwa choti munthu amene anamva maitanidwe anali ndi mwayi wakuvomera maitanidwe koma anakana (Yohani 5:39-40).
- B. Maitanidwe ankati ndi maitanidwe akunjanso chifukwa iwo amachitika ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.
- i. Maitanidwe amachitika ndi Mau a Mulungu mothandizidwa ndi Mzimu Woyera mwa mphamvu yomwe imatsogolera ku chipulumutso (1 Akolinto 23-24).
 - ii. Maitanidwe amphamvu amalozera ku kuchipulumutso (Machitidwe 13:48).
 - iii. Maitanidwewa amakhala osatha ndipo sachotsedwanso (Aroma 11:29).

2. Kubadwanso mwatsopano

- A. Nkofunikira pachipulumutso. Yesu anauza Nikodemo kuti anafunika kubadwanso mwatsopano; kubadwa mwa uzimu kawiri (Yohani 3:7). Njira in yonenera izi ndi kuti munthu ayenera “kubadwa mwatsopano.” Akhristu onse amabadwa mwatsopano.
 - B. Kubadwa mwatsopano ndi chiyambi chotitsogolera ife kuchipulumutso. Apa ndi pamene ntchito ya chisomo imayamba mwa ochimwa. Ndi pamene Mulungu amapereka mtima watsopano (Ezekieli 36:26-27).
 - C. Kubadwanso mwatsopano kumatitsogolera ife kukulapa ndi chikhulupiliro.
- XII. Kutembenuka mtima: Kulapa ndi chikhulupiliro kapena kutembenuka kutchimo ndi kuyang'ana kwa Mulungu.
1. Chikhulupiliro choona chimatitsogolera ife kukulapa komwe kuri kutembenuka kuchokera kutchimo ndi kuyang'ana kwa Mulungu.
 - A. Kulapa kwenikweni kumafunika kuti munthu adziwe kuti tchimo ndi kugalukira Mulungu, ndipo munthu ameneyu amafunafuna kusiya tchimo lake ndi kukhala okondweretsa Mulungu (Machitidwe 26:20).
 - B. Chikhulupiliro choonadi ndi kukhulupilira Ambuye Yesu mosakaika ngati njira yokhayo yodana ndi tchimo. Tinganenenso kuti Yesu ndi njira yokhayo yomwe tingakhululukidwe nayo (Machitidwe 20:21; Aroma 3:25).

- i. Chikhulupiliro choona sikulapa kokha kochokera m'nzeru zathu zokha, koma kumabereka zipatso mwa munthu pamene iye wavomereza uthenga wabwino. Tinene kuti chikhulupiliro choona chimakhala ndi ntchito zake.
- C. Chikhulupiliro chachipulumutso chimabala kusinthika mwa munthu poyanjanitsidwa ndi kupulumutsidwa. Zosinthikazo ndi zinthu monga:
 - i. Kulapa. Tiyenera kulapa machimo athu. Ndi chinthu chofunikira kwambiri chifukwa kwachuridwa kokwana makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zisanu (65) m'Baibulo (Machitidwe 2:38; Mateyu 3:2; Maliko 1:15; Luka 13:3). Tikati kulapa zikutanthauza kuti kuvomereza machimo athu, munthu amamva chisoni ndi machimo ake ndipo amapempha Mulungu kuti amukhululukire machimo ake. Mpempheni Mulungu kuti akuthandizeni kusachimwa. Kulapa kuyenera kuchokera m'mtima osati pakamwa pokha.
 - ii. Tiyenera kukonda Mulungu zimene zikutanthauza kumvera Iye (Yohani 3:16; Luka 6:46; 1 Yohani 2:3-4). Pakutero timadziwa kuti tsopano tam'dziwa Iye; ngati tisunga malamulo ake. Yense onena kuti "Ndim'dziwa Iye" koma osasunga malamulo ake ndi wabodza, ndipo choonadi sichiri mwa iye. Mverani Mulungu.
 - iii. Pakutumikira (Agalatiya 5:13; Luka 14:26; 2 Akolinto 8:5; I Petro 4:10; Aroma 12:11). Musankhale aulesi m'machitidwe anu; khalani achangu munzimu, tumikiranu Ambuye.
- D. Kulapa sikusiyika ngakhale ife titapulumutsidwa. Ndi zomvetsa chisoni, timachimwa tsiku lililonse ndipo timayenera kulapa tsiku lililonse (Masalimo 51).

XIII. Chiyanjano ndi chiombolo

- 1. Chiyanjano ndi kuchotsa kuopsa kwa tchimo. Zikutanthauza kutha kwa nkondo pakati pa otembenuka mtima ndi Mulungu, ndipo timakhala pa mtendere ndi Mulungu (Aroma 5:10; Aefeso 2:16).
 - A. Pali magawo anayi amagawo achiyanjano (2 Akolinto 5:18-12).
 - i. Mulungu sawerengeranso machimo athu motsutsana nafe. Sitidzalangidwa nthawi yosatha chifukwa cha machimo athu.
 - ii. Amawerengera machimo athu pa Khristu.
 - iii. Khristu amalangidwa chifukwa cha machimo athu.
 - iv. Mulungu akupereka chilungamo cha Khristu kwa ife zomwe zikutanthauza kuti timayanjanitsidwa kwa Mulungu. Iye amatitenga kukhala osachimwa pa machimo athu.
- 2. Chiombolo zimatanthauza kuti ndife omasuridwa ku ukapolo watchimo chifukwa cha dipo lomwe Yesu anapereka pa mtanda. Tisanaomboledwe, tinali akapolo a tchimo, koma tsopano tiri ndi Mbuye watsopano.
 - A. Ukapolo wa tchimo ndi oona. Timaona mbiri ya munthu pochimwa nthawi zonse (Genesis 3 ndi 4). Chipangano Chakale ndi Chatsopano chimasonyeza kuchimwa kosalekeza kwa munthu
 - i. Ndingaliro zonse za munthu zinali zochimwa (Genesis 6:5)

- ii. Pachimake penipeni pa tchimo ndi pamene anthu anapha Yesu Mwana wa Mulungu pa mtanda.
 - iii. Ndichifukwa cha ukapolo wauchimo kuti Yesu anadza kudzatiombola ife.
- B. Mpulumutsi wathu ndi Yesu yemwe analipira dipo kuti tikawomboledwe kunsinga za uchimo. Iye amatiombola ku:
- i. Kuzochimwa zonse (Tito 2:14)
 - ii. Kukukakamira kwa tchimo (Aroma 6:18, 22)
 - iii. Kutemberero la lamulo (Agalatiya 3:13)
 - iv. Kunsinga za lamulo (Agalatiya 4:5)
 - v. Imfa (Yobu 5:20)
 - vi. Gehena (Masalimo 49:15)
3. Chiombolo zikutanthauza kuti kugulidwa ku ukapolo, koma mtengo (dipo) wogulira unali waukulu kwambiri.
- A. Mtengo wa mwazi wa Yesu (1 petro 1:18-19)
 - B. Yesu anadza pa dziko lapansi kudzatiombola (Maliko 10:45)
 - C. Lamulo linatipanga ife kulandira imfa yosatha (Aroma 6:23). Zofunika zonse za lamulo; komanso zofunika zonse za chilungamo zinakwaniritsidwa ndi nsembe ya Yesu (Agalatiya 3:13). Mulungu analandira nsembe ya Yesu chifukwa cha tchimo lathu. Tinenenso kuti Yesu analangidwa chifukwa cha machimo athu kuti tikakhulukidwe.
4. Tinalengedwa kuti tikhale ndi chiyanjano ndi Mulungu, koma tinasankha kuphwanya chiyanjano chimenechi pochimwa. Yesu amatikonda kwambiri pakutero anatiombola ife pothira nsembe ya mwazi wake. Anachotsa mwinjiro (mkanjo) wa machimo pakutiveka ife mwinjiro woyera watsopano wachilungamo chake.
- XIV. Chilungamitso chimatanthauza ntchito ya lamulo ya Mulungu imene Iye amalengeza ochimwa kukhala olungama chifukwa chilungamo changwirowo cha Yesu Khristu. Tingatinsu Mulungu amalengeza ochimwa kukhala osachimwa chifukwa cha ntchito ya Yesu. Yesu amatipatsa ife Chilungamo chake chimene amatilungamitsira ife. Chilungamitso chimatsutsana ndi chiweruzo.
- 1. Magawo ndi chikhalidwe cha chilungamitso (Aroma 3:21-26)
 - A. Mulungu amakhulukukira ochimwa; amakhulukukira machimo ake onse akale, atsopano ndi amtsogolo. Ndi tchito yochitika kamodzi (Yesaya 44:22; Aheberi 10:14).
 - i. Ngakhale timakhulukidwa nthawi zonse, timayenera kulapabe ndi kufunafuna chitsimikizo cha chikhulukukiro cha machimo athu omwe ife timachimwa tsiku lililonse.
 - ii. Kukhala mwana wa Mulungu. Zotsatira za chilungamitso chathu timakhala ana a Mulungu ndipo timakhala ndi ufulu monga ana pakukhalanso ndi ufulu wa cholowa chosatha chomwe chiri kumwamba (Aefeso 1:5; 1 Petro 1:4).
 - a. Kukhala kwathu ana a Mulungu kumakhala m'chifuniro cha Mulungu (Aefeso 1:4)

- b. Kukhala ana a Mulungu kumatipanga ife kukhala ndi maufulu ambiri. Timakhala ndi cholowa ndi Khristu.
- B. Kukhala m'khristu kumaposa kukhululupilira ziphunzitso zosiyanasiyana. Akhristu timakhala pamodzi ndi Khristu. Kunena kuti tiri mwa Khristu zikutanthauza kuti:
- i. Tiri ndi madalitso onse auzimu (Aefeso 1:3)
 - ii. Ndife osankhidwa (Aefeso 1:4)
 - iii. Timakhala pafupi ndi Mulungu (Aefeso 2:13)
 - iv. Timalengedwanso mwatsopano (Aefeso 2:20)
 - v. Timakonedwa ndi Mulungu (Aroma 8:39)
 - vi. Ndife amodzi (Agalatiya 3:28)
- C. Munthu aliyense amakhala mwa Adamu (m'tchimo) kapena mwa Yesu. Timakhala ana a Mulungu kapena ana a Satana.
- i. Pakukhala mwa Adamu zikutanthauza kuti kukhala m'mene ife tinabadwira. M'mene muli:
 - a. Tchimo ndi imfa (Aroma 5:17)
 - b. Timakhala m'kwiyo wa Mulungu (Aroma 5:18)
 - c. Moyo wathu umakhala wosamvera Mulungu (5:19)
 - ii. Kukhala mwa Yesu kukutanthauza:
 - a. Tinapachikidwa pamodzi ndi Khristu ndipo machimo athu akale anafa nao pamodzi.
 - b. Ife ngati akhristu sindifenso akapolo a tchimo (Aroma 6:12)
 - c. Ndife akufa mumzimu (6:11)
 - d. Tchimo siridzachita ufumu pa ife (Aroma 6:12)
- D. Zooni ndi zakuti timachimwabe, koma osati nthawi zonse. Timayesetsa kusachimwa ndipo nthawi zambiri timapambana. Tchimo sirichita ufumu m'moyo wathu; m'malo mwake timayesetsa kukondweretsa Mulungu.
- XV. Chiyeretso ndi ntchito ya Mzimu Woyera momwe timayeretsedwa m'mitima yathu nthawi zonse. Chiyeretso zimatanthauza kugonjetsedwa kwa mphamvu ya tchimo pa moyo wathu.
1. Ntchito ya chiyeretso imayambika pamene ife talungamitsidwa ndipo nthawi imene ife tapangidwa kukhala wolungama ndi Mulungu. Izi zimachitika nthawi imene tapulumutsidwa ndi kubadwanso mwatsopano.
 - A. Chiyeretso ndi ntchito yopitilira, pamene Mzimu Woyera ukutiteteza ku mphamvu ya tchimo. Pakutero Mulungu amatipanga ife pang'ono ndi pang'ono kufanana ndi Khristu (1 Atesolonika 4:3-4,7)
 - B. M'moyo uno sitikhalilatu angwiwo opanda tchimo (1 Yohani 1:8).
 - C. Timakhala angwiwo oyeretsedwa opanda tchimo pamene ife timwalira (Aheberi 12:23).
 2. Chiyeretso ndi ntchito yovuta, koma kusinthika kwa munthu ndi umboni kuti munthuyo ndi opulumutsidwa (Akolose 3:1-10).
 - A. Chilungamitso ndi ntchito ya Mulungu yekha.
 - B. Chiyeretso ndi ntchito ya Mulungu komabe munthu ali ndi ntchito yake. Timadalira Mulungu kuti ntchito yathu ikhale yabwino. Umu ndi m'mene timagwilira ntchito yathu ya chipulumutso ndi mantha ndi kunjenjemera (Afilipi 2:12).

- C. Tiyenera kuchilimika kuti tiyeretsedwe. Tiyenera kulimbana ndi umunthu wathu wakale, ndi kulora umunthu watsopano (Aefeso 4:20-32).
- D. Chiyeretso chimatitsogolera ife ku ntchito zabwino. Si ntchito zangwiro komatu ndi zabwino chifukwa zimachokera ku chikondi cha Mulungu ndi chikhulupiliro mwa Iye (Aheberi 11:6).
- i. Ntchito zabwino zimenezi zimachitika mogwirizana ndi chifuniro chake (Yakobo 2:8).
3. Akhristu okha ndi amene amagwira ntchito zabwino. Ntchito za osakhulupilira zimakhala ndi uchimo chifukwa sizikhala ndi mzimu wa chikondi cha Mulungu ndipo sizichitika kuti zipereke ulemelero wa Mulungu. Ntchito zao zabwino sizingawapange iwo kulandira moyo wosatha.
 4. Akhristu ayenera kuchita ntchito zabwino. Izi ndi zizindikiro zoti ndi opulumutsidwa (Yakobo 2:14, 17, 18). Dziwani kuti ntchito zabwino zizidzakupulumutsani komatu zimangotitsimikizira kuti ndife opulumutsidwa ndi mphatso yaulere ya Khristu.
- XVI. Chipiliro cha oyera mtima ndi ntchito yopitilira ya Mzimu Woyera mwa okhulupilira kutsimikizira kuti okhulupilira adzafika mpaka chimaliziro. Zikunthauza kuti opulumutsidwa amakhalabe opulumutsidwa mpaka kumwamba. Sadzataya chikhulupiliro chake (Yohani 10:28; Afilipi 1:6).
1. Pamene tapulumutsidwa, timakhala ana a m’banja la Mulungu, ndipo timakhala ndi maufulu monga ana. Ndife olova m’ malo pamodzi ndi Khristu. Kukhala ana a Mulungu ku nthawi zosantha. Tidzakhalabe ana a Mulungu (Aroma 8:15-17).
 2. Palibe chingatilekanitse ndi chikondi cha Mulungu (8:38-39).
- XVII. Chiphunzitsa cha Mpingo ndi njira za Chisomo
1. Mpingo wapamaloponse (Eklezia) ndi okhulupilira onse padziko lapansi. Si nyumba zomwe ife timapempheramo ayi, mpingo ndi anthu okhulupilira. Akhristu onse ndi ziwalo za mpingo umodzi. Khristu ndi amene akulamulira mpingo wake (Aefeso 5:23; Akolose 1:18, 24).
 2. Mau oti mpingo amatanthauzanso magulu a wanthu omwe amakumana m’ malo osiyanasiyana ngakhalenso m’nyumba (Aroma 16:5, 23).
 3. Mpingo ndi gulu la okhulupilira omwe amakumana pamodzi. Mpingo oona umachita zinthu zitatu izi, ndipo uyenera kuzichitadi:
 - A. Chopambana kwambiri ndi “kulakira Mau a Mulungu” (1 Yohani 4:1-3 ndi 2 Yohani 9. Kumbukirani kulalikira zomwe Baibulo likunena.
 - B. Kupereka Masakarameti oyenera (Mateyu 28:19; 1 Akolinto 11:23-30)
 - C. Kupereka mwambo (Chidzudzuro) (Mateyu 18:18; 1 Akolinto 1:1-5).
 4. Baibulo limatiphunzitsa kuti Mpingo:
 - A. Ukhale ogwirizana Yohani 17:21 ndi Aefeso 4:4-6)
 - B. Ukhale woyera (Exsodo 19:6 ndi Petro 2:9)
 - C. Ukhale wa pamaloponse. Pali mpingo umodzi okha; ndipo okhulupilira onse ali gawo la mpingowu. Tikati mpingo wa pamaloponse sikuti tikugwirizana ndi

- ziphunzitsa za mpingo wa Katolika. Kulibe mipingo yomwe mukuionayi kumwamba; kuli akhristu okha oona mtima (Masalimo 2:8; Chibvumbulutso 7:9).
- D. Ukhale oima pa choonadi basi (2 Timoteo 1:13 ndi Tito 2:1)
5. Ulamuliro ndi mphamvu ya mpingo
- A. Khristu ndiye Mutu wa mpingo ndi ulamuliro wonse. Yesu ndiye olamulira (Mateyu 23:10 ndi 1 Akolinto 12:5-6).
- B. Atumiki onse a mpingo ali pansa pa ulamuliro wa Khristu (Machitidwe 14:23)
- i. Akulu ampingo ank'alalikira ndi kuphunzitsa (1 Timoteo 5:17)
- C. Mphamvu ya mpingo ndi ya mzimu chifukwa imaperekedwa ndi Mzimu Woyera (Machitidwe 20:28)
- D. Mphamvu ya mpingo imachitidwa mwa mzimu (2 Akolinto 10:4)
- E. Mphamvu za mpingo ziri m'njira zitatu:
- i. Mpingo uli ndi mphamvu zophunzitsa. Mpingo uyenera kuteteza choonadi pophunzitsa mibadwo mibadwo pakuteteza motsutsana kumphamvu zonse zakusakhulupilira (1 Timoteo 1:3-4; Tito 1:9-11).
- a. Mpingo ulalikire Mau a Mulungu mosalekeza pakati pa anthu a mitundu yonse (2 Akolinto 5:20); 1 Tomoteo 1:3-4).
- ii. Mpingo uli ndi mphamvu yakudzilamulira okha pokhazikitsa malamulo a Khristu pakati pao (Machitidwe 20:28). Mpingo uli ndi mphamvu yakudzuzura (1 Akolinto 5:2, 7, 13). Awa ndi machimo obisika ngakhalenso osabisika (Mateyu 18:15-18).
- iii. Mpingo uli ndi mphamvu zogwira ntchito zachifundo. Izi zikutanthauza kuthandiza osauka ndi amasiye (Yakobo 1:27; Maliko 14:7; Machitidwe 11:29).
6. Njira za chisomo; Mau a Mulungu ndi Masakaramenti.
- A. Mau a Mulungu ndi chinthu chopambana pa njira ya chisomo.
- i. Mau ndi Mzimu. Pamene Mzimu Woyera umagwira ntchito yake umapangitsa Mau a Mulungu kugwira ntchito m'mitima yathu (1 Akolinto 2:10-14).
- B. Masakaramenti
- i. Nthawi ya Chipangano Chakale Masakaramenti awiri anali Mdulidwe ndi Pasaka. Onse anali Masakaramenti a mwazi mogwirizana ndi Chipangano Chakale.
- ii. Chipangano Chatsopano chiri ndi Masakaramenti awirinso omwe ali Ubatizo ndi Mgonero wa Ambuye omwe sakhudzana ndi mwazi. Thupi ndi mwazi wa nsembe ya Khristu ndi zokwanira kwa onse okhulupilira ndipo nsembe zonse za mwazi sizifunikanso.
- C. Ubatizo unakhazikitsidwa ndi Khristu ataukitsidwa kwa akufa (Mateyu 28:19). Akhristu onse akulamulidwa kubatizidwa ndi madzi (Machitidwe 2:38; Machitidwe 8:36).
- D. Yesu anakhazikitsanso Mgonero wa Ambuye iye asanamwalire. Mkate umayimira chikho cha mwazi wa Khristu. Ichi ndi chizindikiro cha imfa ya Khristu ndipo timakumbukutsidwa phindu la nsembe yake (1 Akolinto 11:26).
- i. Kupezeka kwathu pa Mgonero zimayimira kutenga nao gawo kwathu pa imfa ya Khristu, ndi kupezeka kwa okhulupilira m'moyo ndi mphamvu za Mbuye woukitsidwa.

- E. Mgonero wa Ambuye ndi chindindo chachitsimikizo chachipulumutso chathu kupyolera m'nsembe ndi kuukitsidwa kwa Yesu.
- F. Mgonero wa Ambuye uchitike kwa okhulupilira okha omwe akuona kufunika kwake kwa Mzimu. Ana omwe sanafike pamsinkhu wozindikira ndi iwo amene sanavomereze Khristu asaloredwe kudya nawo Mgonero.
 - i. Ngakhalenso akhristu akale ayambe adziyesa okha asanadye Mgonero (1 Akolinto 11:28-32).

XVIII. Chiphunzitso cha zinthu za chimaliziro

1. Imfa ya kuthupi ikutanthauza imfa ya thupi lathu; wina aliyense adzafa pokhapokha Yesu adzampeze iye akanali ndi moyo (Machitidwe 3:1-2) ndi 1 Atesolonika 4:17). Imfa ya kuthupi ndiyosiyana ndi imfa ya mzimu omwe sumafa (Mateyu 10:28).
 - A. Pamene munthu amwalira thupi ndi mzimu zimalekanitsidwa (Mlaliki 12:7).
 - B. Imfa ndi zotsatira za tchimo ndipo ndi chilango cha tchimo (Aroma 5:12).
2. Kubweranso kwachiwiri kwa Yesu kukunenedwa kokwana mazana atatu ndi khumi ndi mphambu zitatu m'Chipangano Chatsopano. Nthawi yakubwera kwake palibe adziwa choncho musakhulupilire amene amanena kuti akudziwa za tsiku la kubwera kwake (Maliko 13:32).
 - A. Nthawi ino kubwera kwake kuri m'mphamvu zake (24:30)
 - B. Iye adzabwera kudzakhazikitsa nthawi ya mtsogolo yomwe iri nthawi yosatha. Adzachita izi pamene: chiukitso cha akufa ndi chiweruzo chomaliza zidzachitika (1 Atesolonika 4:13 ndi Chibvumbulutso 22:12).
 - i. Baibulo limatiuza kuti pakubwera kwake kwa Khristu akufa adzauka ndipo iwo okhala ndi moyo adzakwatulidwa pamodzi mlengalenga (1 Atesolonika 4:13).
 - ii. Matupi aokhulupilira ndi osakhulupilira adzaukitsidwanso (Danieli 12:2).
- C. Nthawi ya chiukitso ndi pamene Khristu adzabwera ndipo panthawi yomweyo padzakhala chimaliziro (Yohani 5:25-29).
 - i. Palibe amene akudziwa pamene izi zidzachitika (Mateyu 24:36).
3. Chomwe chimachitika munthu akamwalira nthawi ino izi zisanafike: kumwamba kwatsopano, chiombolo cha matupi ndi chiweruzo chomaliza.
 - A. Matupi onse amabwerera kufumbi ndi kuonongeka (Genesis 3:19).
 - B. Mizimu yathu imasungidwa komwe ife tidzapita mpaka chimaliziro ndi Gehena omaliza.
 - i. Mizimu ya wokhulupilira imakhala yangwiro ndipo imakhala ndi Mulungu (2 Akolinto 5:8; Afilipi 1:23).
 - ii. Mizimu ya osakhulupilira imakhala kumalo ozunzika (Luka 16:22-24)
4. Chiweruzo chomaliza ndi momwe zidzakhaliwe
 - A. Chiweruzo chomaliza chidzachitikadi (Machitidwe 17:31)
 - i. Yesu adzakhala oweruza (Yohani 5:27). Angelo ndi amene adzamuthandizire (1 Akolinto 6:2-3).
 - ii. Chiweruzo chidzachitika chiukitso chitangochitika (Yohani 5:28-29).

- iii. Mulingo wachiweruzo udzakhala Baibulo lomwe liri bvumbulutso la Mulungu. Mulungu adzaweruzo munthu monga mwa ntchito zake pakupita iye Kumwamba kapena ku Gehena. Padzakhala mphatso zosiyanasiyana kwa olungama (Mateyu 11:22, 24; Luka 12:47, 48; Yohani 14:2).
- B. Chomwe chidzachitikira anthu
- i. Chomwe chidzachitikira ochimwa
 - a. Iwo adzatumizidwa ku Gehena komwe kuli kumalo amazunzo (Mateyu 13:42; Chibvumbulutso 20:14, 15).
 - b. Amazunzika pamene iwo amwalira (Luka 16:23-24, 28).
 - c. Mazunzo awo sadzatha ku nthawi zosatha (Mateyu 25:46, Maliko 9:48).
 - d. Sizidzatheka kuchoka ku Gehena kupita ku Paradaizo (Luka 16:26).
 - ii. Chomwe chidzachitika kwa olungama
 - a. Chilengedwe chatsopano chidzakhazikitsidwanso. Kumwamba ndi dziko lapansi zidzalengedwanso kuchoka ku chikale (Masalimo 102:26-27; Chibvumbulutso 21:1).
 - b. Kumwamba ndi kosatha (Luka 1:33; Aroma 2:7)
 - c. Mphoto ya oyera mtima ndi moyo opanda mavuto ndi chisokonezo. Tidzakhala mu ulemelero ndi Mulungu, Aroma 8:18. Tidzakhala ndi Mulungu ku nthawi zosatha (Chibvumbulutso 21:3; Aheberi 1:12).